PHUNZIRO LA 61

1. Kodi abusawo ankateteza bwanji nkhosazo usiku?
-Usiku usanafike, abusawo ankamanga linga la miyala kapenga minga mozungulira pa malopo ndipo ankayika khomo limodzi.

2. Lingalo likatha, abusawo ankazikusila nkhosa zawozo mkati mwa lingalo, kodi nanga iwo ankagona kuti?
-Ankagona pabwalo.

3. Kodi chifukwa chiyani abusawo ankagona pa bwalo?
-Kuti ateteze nkhosa zimene zinkakhala zili mu lingalo.

4. Kodi Yesu ankatanthawuza chiyani pamene ankalankhula kuti Iye ndi khomo la nkhosa?
-Yesu ankatanthawuza kuti Iye ndi Njira imene ife tingapulumukire ku imfa.

5. Kodi nkhosa za Yesu ndi ndani?
-Anthu amene akudziŵa kuti tchimo lawo likuyitana imfa, ndipo akupempha Yesu kuti aŵapulumutse.

6. Anthu ena amalankhula kuti pali makomo ambiri opitira kwa Mulungu, kodi zimenezi ndi ziwona?
-Limenelo ndi bodza lamkunguniza.

7. Kodi khomo limodzi lokha la Nowa likutikumbutsa ife chiyani za Yesu?
-Ngati m'mene linalili khomo limodzi la chombo cha Nowa, chomchonso Yesu ndilo khomo lokhalo la ku moyo osatha.
-Ngati m'mene anapulumukira ku imfa anthu amene analoŵa m'chombo muja pogwiritsa nthito khomo limodzi, chomchonso anthu amene
akukhulupilira mwa Yesu adzapulumutsidwa ku mfa.

8 .Kodi mbala imene imadza kudzangoba, kupha ndi kuwononga ndi ndani?
-Satana.

9. Kodi chifukwa chiyani Yesu anabwera?
-Yesu anadza kudzatipatsa ife moyo, ndiponso kudzatipatsa ife moyo osatha.

10. Yesu analankhulanso kuti anazikonda nkhosa zache, kodi nanga anati kuti ali akonzeja kuchita chiyani kwa nkhosa zachezo?
-Analankhula kuti ali okonzeka kuzifera nkhosa zachezo.

-Tsiku lina, Lazaro amene ankakhala ku Betaniya, amene anali nzache wa Yesu anadwala.

Tiyeni tiŵerenge Yohane 11:1-6

1-Tsopano munthu wina wache dzina lake Lazaro anadwala. Anali wa m'mudzi wa Betaniya, kumene ankachokera Mariya ndi m'bale wache Malita.
2-Lazaro amene ankadwalayo anali mulongo wache wa Maliya amene anaŵadzodza Ambuye Yesu ndi mafuta onunkhira bwino, napukuta mapazi awo ndi tsitsi lache.
3-Chomcho alongo ache [Lazaro] anatumiza uthenga kwa Yesu nati, "Ambuye, onani amene mumamukonda uja wadwala?"
4-Koma Yesu pamene anamva izi anati, "Kudwala kumeneko sikuli kwa imfa, koma chifukwa cha ulemelero wa Mulungu, kuti Mwana wa Mulungu alemekezedwe nako.
5-Koma Yesu anakonda Malita ndi m'bale wache pamodzi ndi Lazaro.
6-Koma [Yesu] atamva za uthenga wakuti Lazaro akudwala, anakhalabe kumene analiko kwa masiku ena aŵiri.



ndipo anayika chikhulupiliro chawo mwa Iye.
46-Koma ena mwa iwo anapita kwa Afarisi ndikukaŵawuza zimene anachita Yesu.
47-Pamenepo, akuluakulu amsembe, Afarisi anayitanitsa msonkhano wa anthu a bwalo. Ndipo anafunsana kuti, "Kodi tichite chiyani ife? Chifukwa munthu uyu akuchita zizindikiro zambiri.
48-Ngati tikumuleka kupitiriza zimenezi, anthu onse adzamukhulupilira Iye, Kenako Aloma adzabwera ndikudzalanda malo athu pamodzi ndi mtundu wathu."

-Chifukwa chakuti Yesu anamudzutsa Lazaro ku imfa, anthu ena anakhulupilira mwa Yesu ngati Mulungu Mpulumutsi.
-Chifukwa chakuti Yesu anamudzutsa Lazaro ku imfa, anthu ena anachoka ndikukayamba kupanga upo wakuti amuphe Yesu.

-Kodi amene ankafuna kumupha Yesu anali ndani?
-Akulu akulu amsembe ndi Afarisi.

-Kodi ankaŵatsogolera akulu akulu amsembe ndi Afarisi kuti amuphe Yesu anali ndani?
-Satana.

-Kodi chifukwa chiyani akulu akulu amsembe ndi Afarisi ankafuna kumupha Yesu?
-Chifukwa chakuti iwowo anali anthu oyipa kwambiri.
-Chifukwa chakuti anamumvera Satana osakhala Yesu.

-Kodi inu mudzimumvera ndani?
-Satana kapena Yesu?

ni chifukwa chakuti mwandimvera.

42-Ndikudziŵa kuti mumandimvera Ine nthaŵi zonse, koma ndikulankhula izi chifukwa cha khamu la anthuli kuti likhulupilire kuti Inu ndi amene munandituma Ine."

43-Atatha kulankhula zimenezi, Yesu anafuwula ndi mawu akuru, Lazaro, tuluka!"

44-Ndipo omwalirayo anatuluka ali omangidwa miyendo ndi manja ndi msaru za kumanda; ndipo nkhope yache ili yozingidwanso ndi msaru ya mlezo. Ndipo Yesu anati kwa iwo, "Mmasuleni msaru za kumandazo ndipo mulekeni adzipita.

-Kodi Yesu anachita chiyani?

-Yesu anayima pa khomo la manda, ndipo anamulamula Lazaro kuti awuke ku imfa.

-Kodi Lazaro anawuka ku imfa?
-Inde.

-Kodi Yesu anatha bwanji kuperekanso moyo kwa Lazaro amene anamwalira?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi amene analenga moyo onse.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anaganiza zopereka moyo kwa Lazaro amene anamwalira?
-Chifukwa chakuti Yesu ankafuna kuti aŵawonetse anthu onse kuti Mulungu ali ndi mphamvu ngakhale pa imfa.

-Kodi anthu analankhula chiyani Yesu atatha kumudzutsa Lazaro ku imfa?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 11:45-48

45-Chomcho Ayuda ambiri amene anabwera kudzamutonthoza Mariya, anaziwona zimene anachita Yesu,



-Pamene Lazaro ankadwala, azilongo ache, Malita ndi Maliya, anatumiza uthenga kwa Yesu amene ankakhala kutali ndi mudzi wa Betaniya.

-Kodi Yesu anakatha kumuchiza Lazaro ali kulati?
-Inde.

-Kodi Yesu analankhula chiyani za kudwala kwa Lazaro?
-Yesu analankhula kuti kudwala kwa Lazaro sikubweretsa imfa koma kukhala kwa ulemelero wa Mulungu.

-Ngakhale kuti Yesu anamva za kudwala kwa Lazaro, anapitirizabe kukhala kumene analiko kwa masiku ena aŵiri.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu sanapite nthaŵi yomweyo kwa Lazaro atamva kuti iye akudwala?
-Chifukwa chakuti Yesu ankafuna kuti awonetse mphamvu zache zopambana ngati Mulungu Mpulumutsi.

-Zitatha izi, Yesu analankhula kwa ophunzira ache.

Tiyeni tiŵerenge Yohane 11:7-8 ndi 11-16

7-Kenako [Yesu] anaŵawuza ophunzira ache kuti, "Tiyeni tipitenso ku Yudeya."

8-Ophunzira achewo anayankha kuti, "Mphunzitsi, posachedwapa, masiku apitaŵa, anthu ankafuna kuti akugendeni ndi miyala kumenekuja, kodi nanga chifukwa chiyani mukufuna kuti mupitenso komweko?"

11-[Yesu anapitiriza kuŵawuza kuti, "Mzathu, Lazaro ali mtulo; koma ndikupita kuti ndikamudzutse iye."

12-Ophunzira ache anayankha kuti, "Ambuye, ngati iye ali mtulo, adzachira."

13-Yesu ankatanthawuza kuti [Lazaro] anali at-

amwalira, koma ophunzira ache ankayesa kuti akulankhula za tulo la chibadidwe

14-Chomcho Yesu anaŵawuza musaŵabisila kuti, "Lazaro wamwalira."

15-Ndipo ndikondwera chifukwa chakuti Ine kunalibeko kumeneko, kuti inu mukhulupilire. Koma tiyeni tipite kwa iye."

16-Tomasi (otchedwa Didimo) analankhula kwa ophunzira anzache kuti, "Tiyeni tonse titsagane ndi Iye kumeneko, kuti tikafere pamodzi!"

-Kodi chifukwa chiyani ophunzira a Yesu ankawopa Iye ataŵawuza kuti abwelerenso ku Yudeya?
-Chifukwa chakuti Ayuda a ku Yudeya anayesapo kumugenda Yesu ndi miyala.

-Yesu ataŵawuzanso ophunzira ache kuti Lazaro wamwalira, ophunzira achewo sanamumvetsetse bwino Iye.

-Ophunzira a Yesu ankaganiza kuti Iye akaŵalora atsogoleri a Ayuda kuti akamuphe Iye kuti akakhale limodzi ndi Lazaro.

-Izi, sizimene ankatanthawuza Yesu.

-Kodi chinachitika ndi chiyani Yesu atabweleranso ku Betaniya pamodzi andi ophunzira ache?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 11:17-22

17-Pofika ku Betaniya, Yesu anamupeza Lazaro atakhala kale m'manda kwa masiku okwana anayi.

18-Mudzi wa Betaniya unali pafupi ndi mzinda wa Yelusalemu (osakwana 2 mayilosi),

19-ndipo Ayuda ambiri anadza kwa Malita ndi Mariya kudzaŵatonthoza chifukwa cha imfa ya mulongo wawo.



m'mene amamukondera ite!"

37-Koma ena mwa iwo anati, "Kodi ameneyu ndimayesa ndi amene anamuchiza munthu osawona uja? Kodi sizinakatheka kumuchiza Lazaro?"

38-Zimenezi zitamukhudza Yesu chomchija, anafika ku manda. Linali phanga ndipo mwala unayikidwa pamenepo.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu analira atafika kumanda a Lazaro?
-Chifukwa chakuti Iye anadandawula kwambiri powona anthu ena akulira.

-Mulungu ali adandawula kwambiri chifukwa chakuti muli tchimo m'dziko muno.
-Mulungu ali odandawula kwambiri chifukwa chakuti muli imfa m'dziko muno.

-Anthu akavulala, Mulungu amadandawula.
-Anthu akadwala, Mulungu amadandawula.

-Ichi ndi chifukwa chakuti Iye ndi amene analenga anthu onse, ndipo amaŵakonda anthu onse.

-Kodi kenako Yesu anaŵawuza chiyani anthu?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 11:39-44

39-Yesu anaŵawuza anthu kuti, "Chotsani mwalawo!" Koma Malita, Mulongo wache wa munthu womwalirayo, anati, "Ambuye! Tsopano wayamba kuwola, patha masiku anayi chimuyikireni m'manda."

40-Kenako Yesu anati, "Kodi sindinakuwuze kuti ukakhulupilira, udzawona ulemelero wa Mulungu?"

41-Anthu aja anachotsa mwala uja. Kenako Yesu anayang'ana kumwamba nati, "AMBUYE, Ndikukuyamika-

Tiyeni tiŵerenge Yohane 11:27

27-Iye anayankha kuti, “Inde Ambuye! Ine ndikukhulupilira kuti Inu ndi Kilisitu, Mwana wa Mulungu, wakudza m’dziko la pansi.”

-Kodi Malita ankakhulupilira kuti Yesu ndi Mulungu Mpulumutsi?
-Inde.

-Kenako, Malita anamuyitana m’bale wache Mariya.

Tiyeni tiŵerenge Yohane 11:28-38

28-Malita atalankhula zimenezi, anabwelera ndipo anamuyitanira pambali Mariya, m’bale wache. Chomcho anamuwuza kuti, “Mphunzitsi wafika ndipo akukuyitana.”
29-Maliya atamva izi, anadzuka ndikuturuka panja mwansangansanga kukawonana naye.
30-Yesu anali asanafike m’mudzimo, koma analibe ku malo kumene anakomana ndi Malita kuja.
31-Ayuda amene anali m’nyumba muja kumamutonthoza iye, atadabwa ndi changu chimene anachita poturuka m’nyumbamo, anamutsatira, ankaganiza kuti akupita ku manda kukalilira komweko.
32-Mariya atafika kumene kunali Yesu ndipo atamuwona Iye, anagwa pa mapazi ache nati, “Ambuye, Inu munakakhala kuti munali kuno, mulongo wanga sibwenzi atamwalira.’
33-Yesu atamuwona iye akulira pamodzi ndi Ayuda amene anatsagana naye, anakhudzidwa kwambiri mu uzimu, ndipo anavutika mu mtima.
34-Iye anaŵafunsa iwo kuti, “Kodi mwamuyika kuti?” Iwo anayankha kuti, “Ambuye, tiyeni mukakuwone.”
35-Yesu analira.
36-Kenako Ayuda analankhula kuti, “Tawonani



20-Pamene Malita anamva kuti Yesu akubwera, anapita kukamuchingamira, koma Mariya anatsala ku nyumba.
21-Malita anati kwa Yesu, “Munakakhala kuti munali kuno, mulongo wanga sibwenzi atamwalira.
22-Koma ndikudziŵa kuti ngakhale tsopano, Mulungu adzakupatsani china chilichonse chimene mungampenphe.”

-Kodi mulongo wache wa Lazaro, Malita, analankhula chiyani kwa Yesu?
-Malita analankhula kuti Yesu anakakhala kuti anali komweko, sibwenzi Lazaro atamwalira.

-Malita ankaganiza kuti Lazaro anakakhalabe ndi moyo Yesu anakakhala kuti anali kumeneko chifukwa chakuti Iye anakamuchiza Lazaro.

-Kodi kenako Yesu analankhula chiyani kwa Malita?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 11:23-24

23-Yesu anati kwa iye, “Mulongo wako adzawuka.”
24-Malita anayankha kuti, “Ndikudziwa kuti adzawukanso pa tsiku lomaliza.’

-Yesu anamuwuza Malita kuti Iye akamuwukitsa mulongo wache, Lazaro.

-Kodi Malita anamvetsetsa?
-Ayi.

-Malita anamuwuza Yesu kuti iye ankadziŵa kuti Lazaro adzakhalanso ndi moyo pa tsiku lomaliza.

-Kodi Malita ankatanthawuza chiyani ponena kuti Tsiku

lomaliza?
-Pa tsiku lomaliza lidzakhala tsiku limene anthu onse akufa adzawukenso kumanda.

-Pa tsiku lomaliza lidzakhala tsiku limene anthu onse akufa adzawukenso kumanda kuti aweruzidwe ndi Mulungu.

-Pa tsiku lomaliza, Mulungu adzaŵaweruza anthu onse chifukwa cha machimo awo.

-Malita ankaganiza kuti Yesu adzamudzutsanso mulongo wache, Lazaro, pa tsiku lomaliza.

-Kodi Yesu ankatanthawuza zimenezi?
-Ayi.

-Kodi Yesu anayankha chiyani kwa Malita?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 11:25a

25a-Yesu anati kwa iye, "Ine ndi Ine kuwuka ndi Moyo.

-Kodi Yesu analankhula chiyani kwa Malita?
-Yesu anati kuti Iye ndi Kuwuka ndi Moyo.

-Yesu ankamuwuza Malita kuti Lazaro sayenera kuyembekezera pa tsiku lomaliza kuti awukitsidwe.

-Kodi chifukwa chiyani Lazaro sayenera kuyembekezera pa tsiku lomaliza kuti awukitsidwe?
-Chifukwa chakuti Yesu anali pomwepo, ndipo Iye ndi Kuwuka ndi Moyo.

-Yesu anali ndi mphamvu zopereka moyo kwa anthu amene ali ndi moyo ngakhale omwalira.



-Kodi Satana ndi ziwanda zache angapereke moyo kwa anthu akufa?
-Ayi.

-Kodi nanga angero angapereke moyo kwa anthu akufa?
-Ayi.

-Kodi ndi ndani yekha amene angapereke moyo kwa anthu akufa?
-Yesu amene ali Mulungu.

-Kod kenako Yesu analankhulanso chiyani kwa Malita?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 11:25b-26

25b-okhulupilira Ine, ngakhale amwalire, adzakhala ndi moyo;
26-ndipo aliyense okhala ndi moyo, nakhulupilira Ine, sadzamwalira nthaŵi zonse. Kodi ukhulupilira ichi?"

-Yesu analankhula kuti aliyense okhulupilira mwa Iye adzakhalabe ndi moyo ngakhale amwalira.

-Kodi munthu angakhale bwanji ndi moyo atamwalira?
-Kodi Yesu ankatanthawuza chiyani?
-Yesu ankatanthawuza kuti aliyense okhulupilira mwa Iye sadzafa pamaso pa Mulungu ngakhale kuti thupi lache lidzafe.

-Yesu ankalankhula kuti aliyense okhulupilira mwa Iye, mzimu wache udzapita kumwamba kukakhala ndi Mulungu ngakhale kuti thupi lache lidzafe.

-Kodi kenako Malita anayankha chiyani kwa Yesu?